# Sigillum Dei Vivi

## Chidindo Cha Mulungu Wopatsa Moyo

*Pemphoroli ndi mphatso yapadera imene Mulungu Atate anapereka kwa Mneneri, Maria Divine Mercy, kuti litetedze ana onse a Mulungu.*




*Onse amene adzapemphere pemphoroli adzakhala wotetedzedwa pamodzi ndi mabanja awo, mu nthawi yoyembekezera kubwera kwa chiwiri kwa Ambuye Yesu*

Galamukani ndikulandira chidindo, Chidindo cha Mulungu Wopatsa Moyo. Pempherani pemphoroli (33) kuti mulandire Chidindo changa ndipo chivomereni mwa chikondi, mwansangala ndi mothokoza.

**Mulungu Atate wokondeka, ine ndabwera pamaso panu kuti ndilandire Chidindo chanu cha chitetedzo. Thupi langa ndi mzimu wanga ndimbali imodzi ya Umulungu wanu. Ndagwada pansi kuthokoza, kuchokera pansi pa mtima wanga ndipo ndikulonjeza kumvera inu, Mulungu Atate anga wokondeka. Ndikukupemphani kuti munditetedze ine ndi abale anga onse ndi Chidindo chanu Choyera. Ndikupereka moyo wanga kuntchito yakutumikira inu nthawi zonse. Ndimakukondani Atate. Ndikukutonthozani Atate, chifukwa cha zinthu zomwe zikuchitika dziko la pansi munthawi yino. Ndikupereka Thupi, Magazi, Mzimu ndi Umulungu wa mwana wanu wokondeka ngati nsembe yopepesera machimo a dziko lapansi komanso ngati njira yopulumutsira ana anu onse. Amen**

Bwerani ana anga musachite mantha. Khulupilirani mwa ine, Atate anu okondeka, amene analenga aliyense mwa inu, mwa chikondi. Ndimadziwa aliyense wa inu payekha payekha ndipo palibe aliyense mwa inu amene ndimamukonda koposa mnzake. Chifukwa cha ichi sindifuna kutaya ngakhale mmodzi wa inu, kwa satana. Chonde pitirizani kupemphera kolona ya chifundo mosalekeza. Tsiku lina liri kubwera pamene mudzamvetse kuti ndichifukwa chani, mukuyenera kuzunzika.

Ndine Atate anu akumwamba

*Mulungu Atate Amphamvu Zonse*